# Nkhuku ndi Nkhwazi

Ann Nduku
Wiehan de Jager
Sitwe Benson Mkandawire
3
Chichewa ny

Panali-panali, nkhuku ndi nkhwazi anali paubwenzi. Anakhala mumutendere ndi nyoni zina. Kulibe kanyoni kamene kanali kumbululuka.

Tsiku limodzi, kunali njala kwamene anali kukhala. Nkhwazi anali kuyenda kutali kuti apeze cakudya. Anabwelera olema kwambiri. “Kufunikira njila ina yapafupi mumayendedwe” Nkhwazi inatelo.

Mumawa mwace, nkhuku inali ndi cocita. Anayamba kudoba weya wa nyoni iliyonse wamene unagwa. “Tiyeni titungile pamodzi namaweya yamene tili nayo” inatelo nkhuku. “Mwina ici cizakhala capafupi kuyenda”.

Nkhwazi ndiye anali cabe na nyeleti yotungila pamunzi, iye anayambilira kusoka. Anazipangila maweya yabwino-bwino nakumbulululuka pamwamba pa nkhuku. Nkhuku inabweleka nyeleti koma analema kutunga. Anasiya nyeleti yotungila pa kabati ndiponso anayenda kukakonza cakudya ca ana.

Nyoni zina zinamuona nkhwazi kubululuka. Anafunsa nkhuku kuti iwabweleke nyeleti kuti azipangile maphapindo yombululukila nao. Posacedwa, kunali nyoni zambili kumbululuka mumwamba.

Pamene nyoni yomaliza inabweza nyeleti yotungila, nkhuku siyinaliko. Ana a nkhuku anatenga nyeleti nakuyamba kuisoweletsa. Pamene analema kusowera, anasiya nyeleti mumcanga.

Mumazulo, nkhwazi anabwelera. Anapempha nyeleti kuti atunge maweya yamene siyanali bwino kucoka paulendo. Nkhuku inasakila nyeleti pakabati, mophikila, ndi panja pa nyumba. Koma nyeleti sinaoneke.

“Ndipaseni tsiku limodzi” Nkhuku inapempha nkhwazi. “Kuti mukakonze maweya yanu nakumbulululukanso kukasakila cakudya”. “Tsiku limodzi cabe” Nkhwazi anatelo. “Ngati siupeza nyeleti, uzanipatsa mwana wako yumozi kukhala malipiro”.

Pamene nkhwazi inabwela tsiku lokonkhapo, anapeza nkhwazi asakila mumucanga kuno nyeleti sanaipeze. Nkhwazi anabwela mwamsanga nakutenga kamwana ka nkhuku kamozi nakuyendanako. Kucoka ija tsiku, nkhwazi ikaonekela cabe, iona nkhuku isakala nyeleti mumicanga.

Ngati mudima wa nkhwazi waonekela kucoka kumwamba, nkhuku icenjeza ana ace. “Cokani poonekela”. Ndiponso iwo akuyankha, “Sindife oputsa, tizathamanga”.

# Global Storybooks

globalstorybooks.net

## Nkhuku ndi Nkhwazi


Ann Nduku
Wiehan de Jager
Sitwe Benson Mkandawire


CC BY